# Malongosoledwe a coonadi ca m'Baibulo

## Za makhalidwe a ana a Mulungu

1. Ana a Mulungu ndiwo olengedwa atsopano
2. Ana a Mulungu amkonda Iye
3. Ana a Mulungu akondana
4. Ana a Mulungu amkhulupirira Iye
5. Ana a Mulungu apatsa
6. Ana a Mulungu amvera
7. Ana a Mulungu agwira nchito
8. Ana a Mulungu awerenga Baibulo
9. Ana a Mulungu amganizira Iye
10. Ana a Mulungu aphunzira kukana
11. Ana a Mulungu auza nthano ya Mulungu
12. Ana a Mulungu azunzika cifukwa ca Iye
13. Ana a Mulungu afuna za tsogolo

Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiriro, ndipo ici cosacokera kwa inu: ciri mphatso ya Mulungu; cosacokera kunchito, kuti asadzitamandire munthu ali yense. Pakuti ife ndife cipangano cace, olengedwa mwa Kristu Yesu, kucita nchito zabwino, zimene Mulungu anazipangiratu, kuti tikayende m'menemo – Afeso 2.8-10

Mbali zina za m'buku iri zinasandulidwa kucokera ku buku ilo: Schoolland, Marian. M. (1962), *Leading Little Ones To God* (21st ed), Wm. B. Eerdmans Publishing Company.

- ©Stephanos Zambia Trust –
www.kudziwazamulungu.com

## 1. Ana a Mulungu ndiwo olengedwa atsopano

*Cifukwa cace ngati munthu ali yense ali mwa Kristu ali wolengedwa watsopano – 2 Akorinto 5.17a*

**Kuwerenga**
Yohane 15.1-5

**Malongosoledwe**
Kodi mukumbukira kuti Adamu ndi Hava anakondwera kwambiri m'munda wa Edeni, iwo asanacimwire Mulungu? Mwina mukumbukira mau a pa mtima omwe tinaphunzira kale, 'Mulungu ndipo adalenga munthu m'cifanizo cace'. Adamu ndi Hava anali osacimwa ndi oyera.
Koma anacimwira Mulungu. Sanamumvere. Ndipo iwo anasanduka pa nthawi ya kucimwa kwao: kucokera ku nthawi iyo, iwo sanali oyera ndipo sanali osacimwa. Anasanduka odzikonda, odzala ndi kuda, okonda mkangano, aumbombo komanso osasangalala kwambiri. Tsono, ife tonse munsi m'mitima yathu, ndife monga iwo. Ndife ocimwa. Nthawi zambiri sitikondwera. Mulungu alephera kuona cifanizo cace mwa ife.
Yesu anabwera kuti macimo athu akhululukidwe, kuti tikhale oyenerera ndi opanda uchimo. Ngati tikhulupirira Yesu ngati Mpulumutsi wathu, Mulungu atipatsa mitima yatsopano; mitima imene ifuna kukhala moyo kwa Iye. Yesu abwera kukhala m'mitimayo yatsopano ndipo zoipa zonse ziyenera kucokamo. Mitima yatsopano ifuna kuti ticita zabwino ndi zoyenerera.
Koma zoipa sizicokamo pa nthawi imodzi! Tisasanduka oyera ndi abwino opanda macimo mwadzidzidzi. Mitima yakale yocimwa ulikonso ndipo mitimayo ifuna kuti ticimwa.
Akristu ayenera kukula. Mulungu afuna kuti tisanduka kukhala monga Yesu. Mudziwa kuti Yesu anali wabwino ndi wokoma mtima kwambiri. Iye anali woyera, wacifundo ndi wacikondi ndipo nthawi zonse anacita zimene Atate wake anafuna kuti azicita. Akristu azikhala monga Iye. Ayenera kukula kuti akhale Akristu abwino kuposa ndi amphamvu kuposa m'mene aliri. Aziyenera kuphunzira kucita cifuniro ca Mulungu. Ayenera kukula amphamvu kumenyera uchimo wa m'mitima yao yakale.
Ngati Yesu akhala m'mtima wanu, ndinu 'olengedwa atsopano' ndipo mudzakhala monga Yesu. Tsegulirani Yesu mtima wanu kuti mtima udzale ndi cikondi cake ndipo Iye adzacotsamo zoipa.
M'maphunziro ena atsogolo tidzaphunzira zina za kukula.

**Kukambirana**
1. Kodi zoipa za m'mitima yathu zicotsedwe bwanji?
2. Kodi m'mtima mwanu muli zoipa zotani zimene ziyenera kucokamo?
3. Kodi mtima watsopano ndi mtima wotani?
4. Kodi munthu wolandira mtima watsopano, angacimwe?
5. Fotokozani 2 Akorinto 5.17a.

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Mulungu, Munalenga kumwamba ndi dziko lapansi. Ndinu Wamphamvuyonse. Muli ndi mphamvu ngakhale kuposa macimo. Nthawi zambiri tikucimwirani. Tikupemphani kuti mutipatse mitima yatsopano imene imenyera uchimo mwa mphamvu yanu. Tikupemphani kuti Ambuye Yesu acotse zoipa zonse za m'mitima yathu, cifukwa Iye anagonjetsa kale macimo onse pamene anafa pa mtanda. Tikupemphani izi m'dzina lanu. Amen.

## 2. Ana a Mulungu amkonda Iye

*Tikonda ife, cifuka anayamba Iye kutikonda – 1 Yohane 4.19*

**Kuwerenga**
Yohane 12.1-3

**Malongosoledwe**
Tsiku lina, pamene Yesu anali pa dziko lapansi, m'modzi wa anzake anamkonzera cakudya cabwino. Simoni wa ku Betaniya anaitana anzake a pa mtima a Yesu: Lazaro amene anakonda kwambiri Yesu, abale a Lazaro (Mariya ndi Marita) komanso anthu ena ambiri pamodzi ndi Yesu ndi ophunzira ake.
Marita anathandiza kukonzera cakudya. Anamva bwino kutumikira Yesu. Anamkonda kwambiri!
Mariya nayenso anakonda Yesu. Iye anaganiza za njira ina yoonetsa cikondi cake. Anabwera ndi botolo la mafuta onnkhira bwino a mtengo wapatali.  Mafuta awo anali mafuta odzola pathupi a mtengo wapatali kwambiri. Mariya anafuna kupatsa Yesu mafutawo apamwamba.
Pamene alendo onse anakhala pansi pa tebulo, Mariye anapita kumbuyo kwa Yesu. Anatsegula botolo nayamba kuika mafuta pa Iye. Anaika ena pa mutu wa Yesu ndi ena pa mapazi ake. Anatsiriza mafuta onse. Anamkonda kwambiri!
Mnunkho wa mafutawo unadzala cipinda. Ndipo Mariya anagwadira pansi Yesu kukapukuta mapazi ake ndi tsitsi lake lalitali ndi looneka bwino.
Anthu ena a alendo anaganiza kuti Mariya anataya mafuta moika mafutawo pa Yesu motere. Koma sanataye. Cinali mphatso yake mwa cikondi. Cinali cinthu capamwamba kwambiri cimene adampatsa. Ndipo Yesu anasangalala.
Lazaro nayenso anakonda Yesu. Mariya, Marita ndi Lazaro anali anzake a pa mtima a Yesu. Kodi mudziwa ndi cifukwa ciani iwo anakonda Yesu kwambiri?
Yesu adakhala m'nyumba yao nthawi zambirimbiri. Iwo anadziwa kuti Yesu ndi wabwino, wacikondi ndi wokoma mtima kwambiri. Adamva mau a Yesu. Anakhulupirira kuti Yesu ndi Mpulumutsi wotumidwa ndi Mulungu. Anakhulupirira kuti Yesu adzacotsa macimo ao, ngakhale pa nthawi iyo, iwo sanadziwe kuti Yesu adzawafera. Iwo anadziwa kuti Yesu awakonda kwambiri. Ndipo cifukwa cace, iwo anamkonda Yesu.
Ife tidziwa kuti Yesu atikonda kwambiri kotero kuti anatifera pa mtanda. Tizimkonda! Tidziwa kuti atikonda ngakhale tsono ndiponso kuti atilondolera nthawi zonse. Ngati ndife ana a Mulungu moonadi, ngati tiri ndi mitima yatsopano ndithu, tikonda Mulungu ndipo tizimkonda koposa.

**Kukambirana**
1. Kodi Mulungu amaticitira ciani tsiku ndi tsiku?
2. Kodi munalandira mitima yatsopano? Kodi ndinu ana a Mulungu ndithu?
3. Kodi tingacite ciani kuonetsa cikondi cathu ca Mulungu?
4. Werengani 1 Yohane 1.19. Kodi ciyambi ca cikondi cathu ndico ciani?
5. Kodi kutanthauza ciani kwa inu kuti Mulungu anatikonda tisanamkonde Iye?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Mulungu wa cikondi, Tikuyamikani kuti ndinu wacikondi. Inu munayamba kutikonda ndipo cifukwa ca Inu tingakukondeni. Osati mwa ife, koma cikondi cathu cicokera mwa Inu. Mutidzale ndi cikondi canu kuti tikukondani moonadi. Mwa Yesu Kristu Mwana wanu wokondedwa, Amen.

## 3. Ana a Mulungu akondana

*Mukondane wina ndi mnzace, monga ndakonda inu – Yohane 15.12*

**Kuwerenga**
1 Yohane 4.7-11

**Malongosoledwe**
Kodi pamene muli kusewera sewero, munena 'Ine poyamba!'?
Mudziwa kuti si cinthu cabwino kulankhula tero.
Cifukwa ciani si cinthu cabwino kulankhula tero? Cifukwa pamene munena 'Ine poyamba!' ndinu odzikonda. Mudzikonda koposa.
Kodi kunyada ndi koipa? Nanga kudzikonda koposa?
O, inde! Mulungu akamba kuti tizikonda Iye koposa. Ndipo Mulungu akamba kuti tizikonda anthu ena monga tidzikonda ife tokha. Uchimo m'mtima wathu utipangitsa kukonda ife mwini kuposa anthu ena onse.
M'mitima ya anthu onse muli kudzikonda. Ngakhale ophunzira a Yesu anadzikonda. Tsiku lina, iwo anafunsa Yesu, 'Ndani adzakhala wopambana m'Ufumu wa Kumwamba?' Ndipo aliyense anafuna Yesu kunena kuti wopambana ndi iye yemwe.
Yesu anayenera kuphunzitsa ophunzira ake kukhala osadzikonda. Tsiku lina anawaphunzitsa phunziro limene iwo sangaiwale konse.
Kunali nthawi ya mgonero: mgonero wotsiriza wa Yesu ndi ophunzira ake. Mgonero unali wosangalatsa. Pamene Yesu ndi ophunzira ake anafika, mgonero unali wokonzedwa. Mapazi a iwo onse anali afumbi, cifukwa ankabvala masandasi cabe. Anaganiza kuti kudzakhala kapolo womwe adzasambitsa mapazi ao. Koma pamene anayang'anira powazungulira, anaona cikho ca madzi ndi coumitsira koma sanaone kapolo. Ophunzira sanafune kucita nchito ya kapolo. Kunalibe m'modzi wa iwo amene anafuna nchito yotere. Ndiye onse anakhala pansi pa tebulo ndi mapazi akuda.
Kenaka Yesu anaimirira. Iye anaika madzi m'mbale nayamba kusambitsa mapazi a ophunzira ake. Ici cinawapangitsa kumva manyazi ndi kuti adalakwa. Ganiziraniko: Yesu, Ambuye wao, Mwana wa Mulungu, anacita nchito ya kapolo.
Pamene Yesu anafika kwa Petro, iye ananena, 'O, iai! Simuyenera kusambitsa mapazi anga!' Komabe Yesu anasambitsa mapazi a Petro. Anasambitsa mapazi a ophunzira ake onse ndipo anawaumitsa ndi coumitsira.
Atatsiriza, Yesu anakhala pansi nanena, 'Mundicha Mphunzitsi ndi Ambuye. Ine ndine Mphunzitsi wanu ndi Ambuye wanu, komabe ndasambitsa mapazi anu. Ndasambitsa mapazi anu kukuonetsani m'mene muzikondanirana.'
Ngati Ambuye wao anawakonda kotero kuti anafuna kukhala Mtumiki wao, iwonso ayenera kukondana. Ndipo ifenso tizikondana. Tiyenera kukhala ngakhale atumiki a anthu ena!
Tiyenera kukula m'cikondi ca kwa anthu ena.

**Kukambirana**
1. Kodi tingadzikweze m'njira zotani?
2. Kodi Yesu anaonetsa cikondi cake m'njira zotani?
3. Kodi tingakondane m'njira zotani?
4. Kodi tingacite ciani kutumikira ndi kusangalatsa anthu ena?
5. Mulungu anena m'Yohane 1.2, 'Iye wakunena kuti akhala mwa Iye, ayeneranso mwini wace kuyenda monga anayenda Iyeyo'. Kodi ndime iyi itanthauza ciani?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wa Kumwambamwamba, Yesu anadzipereka kwa anthu ocimwa kuti iwo apulumuke ku macimo ao. Mwana wanu anakhala ngati Mtumiki. Tiphunzitseni kuti tizikonda ndi kutumikira anthu ena. Mutikhulululukira kudzikonda kwathu. M'dzina la Yesu tikupemphani izi. Amen.

## 4. Ana a Mulungu amkhulupirira Iye

*Koma wokhulupirira Yehova adzapulumuka – Miyambo 29.25b*

**Kuwerenga**
Mateyu 14.24-31

**Malongosoledwe**
Mulungu amasungira zonse. Dziko lonse lapansi lalikuli liri m'manja ake. Mwezi ndi nyenyezi ziri m'manja ake. Amasungira mbalame ndi maluwa. Amasamalira ana ang'ono. Amasamalira inu ndi ine. Amasamalira anthu ake onse ndipo analonjeza kutisamalira nthawi zonse.
Baibulo litiuza nthano ya Petro: tsiku lina iye anacita cinthu codabwitsa pamene anakhulupirira Yesu. Litiuzanso cimene cinacitika pamene analeka kukhulupirira Yesu.
Ophunzira a Yesu anali m'ngalawa pa nyanja. Kunali usiku. Kunali cabe kuwala kwa mwezi komwe kunawaonetsa njira yopita ku mbali ya nyanja. Ndipo kunadza mkuntho. Mphepo inayamba kuomba kwambiri. Inayendetsa ngalawa ku njira ina ndipo mafunde akulu anawaza m'ngalawa. Ophunzira anaopa. Ndipo Yesu sanakhale nao pa nthawi iyo.
Pamene ophunzira anayesa kwambiri kuyendetsa bwato, mwadzidzidzi iwo anaona cinthu ca pa madzi: cinthu coyera ndi cocititsa mantha. Cinali kuyenda. Cinabwera nao. Cifukwa ca mdima, iwo sanakhoze kudziwa kuti ndi ciani. Anaopa kwambiri. Cinthuco coyera cinali cocititsa mantha cuposa mkuntho.
Ndipo kenaka anamva mau: mau a Yesu! 'Osaopa!', Yesu ananena, 'Ndine!'
O, ophunzira anakondwera kwambiri! Sanayenere kucita mantha konse. Yesu anali kubwera nao poyenda pa madzi. Iye anakhala nao nthawi zonse za mkuntho nawasamalira.
Petro ananena, 'Ngati ndinutu, Yesu, ndiloleni kuyenda pa madzi kukumana nanu'.
Yesu anati, 'Idza!'
Petro anasiya ngalawa. Anayang'anira Yesu pamene anaika mapazi ake pa madzi. Ndipo anayenda pa madzi, monga Yesu anacita, mosamira.
Koma madzidzidzi mphepo inaomba koposa. Funde lalikulu linadza pali Petro. Petro analeka kuyang'anira Yesu koma anayang'anira funde. Ndipo anaopa. Anayamba kumira.
'O, Ambuye, ndithandizeni!, iye analira.
Yesu anagwira dzanja la Petro. Anamkweza. Anati, 'Cifukwa ciani sunandikhulupirira?'. Kenaka iwo anapita pamodzi ku ngalawa.
Ndi cinthu codabwitsa kuti Petro anayenda pa madzi moyang'anira Yesu, iai? Anayamba kumira cabe pamene analeka kuyang'anira Yesu ndi kumkhulupirira.
Tiyenera kukhulupirira Yesu nthawi zonse.
Petro sanayenere konse kumva mantha. Anacita cimene Yesu anamuuza kucita. Pamene ticita zimene Mulungu ndi Yesu afuna kuti tizicita, sitiyenera konse kuopa, m'zonse zimene zingacitike. Mulungu analonjeza kutisamalira ndipo amasunga malonjezo ake.
Cikhulupiriro cathu ca m'Yesu ciyenera kukula kuti cikhale colimba koposa.

**Kukambirana**
1. Fotokozani mwacidule cimene cinacitika m'nthano ya Petro.
2. Kukhulupirira kutanthauza kuika ciyembekezo conse mwa Yesu Mpulumutsi. Kodi mumkhulupirira ngati Mpulumutsi wanu?
3. Citanthauzanji kuti cikhulupiriro ciyenera kukula?
4. Kodi tidziwa bwanji kuti Mulungu ndi wokhulupirika?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wokhulupirika, Nthawi zina tingacite mantha. Mutikhululukire kusakhulupirira kwathu. Mutiphunzitse kuti sitiyenera kuopa ngati muli pafupi nafe. Tipatseni Mzimu wanu Woyera kuti tizikhulupirira moonadi. Tikupemphani zonse mwa cisomo, mwa Yesu. Amen.

## 5. Ana a Mulungu apatsa

*Kupatsa kutidalitsa koposa kulandira – Macitidwe 20.35*

**Kuwerenga**
Mateyu 10.42

**Malongosoledwe**
Kupatsidwa mphatso ndi cinthu cokondweretsa, iai? Koma mudziwa kodi, cimene citikondweretsa kwambiri? Kupatsa mphatso kutikondweretsa kwambiri kuposa kulandira. Tingapatse mphatso kwa amai, atate, abale athu ndi anzathu cifukwa tiwakonda. Yesani ndipo mudzaona m'mene inu nomwe mudzakondwera.
Cabwino coposa ndi kuti tikhoza kupatsa kwa Mulungu. Ici citikondweretsa koposa. Kodi mukumbukira m'mene Mariya anapatsa Yesu mafuta onunkhira opamwamba?
Kale kwambiri, pamene Aisrayeli anali anthu apadera a Mulungu, Iye anawauza kumanga Cihema: hema lalikulu m'mene akhoza kumpembedzamo Mulungu. Mulungu anauza Mose mtsogoleri wao za kumangidwa kwa Cihema. Ndipo Mulungu anati, 'Aliyense amene *afuna*, aloledwa kupereka zinthu za Cihema. Mungapatse golide ndi siliva, mungapatse mapulanga, cinsalu cabwino ndi zikopa, mungapatse zobvala za miyala ya mtengo wapatali ndi lubani zabwino.'
Kodi muganiza kuti anthu ambiri anafuna kupatsa Mulungu mphatso za Cihema? O, inde! Iwo onse okonda Ambuye anasangalala kupatsa mphatso zao. Anapatsa zinthu zambirimbiri. Ndipo anapatsa zinthu zao zabwino zoposa. Anapatsa zambiri kotero kuti Mose anayenera kuwauza kuti aleke. Mose anali ndi mphatso zambiri zokwanira kumanga Cihema. Anthu anaonetsa Mulungu kuti amkonda kwambiri. Cifukwa ciani iwo anakondwera kwambiri kupatsa mphatso kwa Mulungu? Cifukwa *Iye* adawacitira zambiri.
Mulungu ndi Wopatsa wamkulu. Zonse zimene tiri nazo, zinapatsidwa ndi Iye. Pamene tipatsa, ndife monga Iye pang'ono. Ndipo ico citikondweretsa. Kodi tingapatse ciani? Ndipo tingapatse yani?
Poyamba, tiyenera kudzipereka konse kwa Mulungu. Ngati ndife ana a Mulungu, tinena kwa Mulungu, 'Ndine wanu, Atate wokondedwa'. Ici ndi codabwitsa koposa. Mulungu aikonda koposa mphatso iyi.
Kenaka, cifukwa tikonda Mulungu, tifuna kupatsa kwa anthu ena. Tifuna kugawa zinthu zathu zabwino. Tipatsa kwa anthu osauka, cifukwa Yesu awakonda. Tipatsa kuthandiza atumiki a Mulungu omwe amafalitsa kulikonse nthano za Yesu. Tipereka mau okoma mtima ndipo ticitira zabwino anthu otizungulira, monga Yesu anacita.
Yesu anati kuti ngati tipatsa kwa munthu wina cifukwa tikonda Yesu, tipatsa kwa Yesu yekha ndithu. Ndi cinthu codabwitsa kuti tikhoza kupatsadi kwa Yesu, monga Mariya anapatsa mafuta onunkhira apamwamba, iai? Ifenso tikhoza kuonetsa Yesu kuti timkonda kwambiri.
Ndipo kupatsa kotero kudzatikondweretsa.
Kupatsa kwathu kuyenera kukula ndi kukula koposa.

**Kukambirana**
1. Patsani zitsanzo zisanu za mphatso zimene tilandira kucokera kwa Mulungu.
2. Kodi cinthu coyamba cimene tiyenera kupatsa kwa Mulungu ndico ciani?
3. Kodi mukonda kupatsa?
4. Cifukwa ciani kupatsa kutisangalatsa?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wakumwambamwamba, Ndinu wacifundo. Munapatsa Yesu Kristu kukhala Mpulumutsi wa anthu ake onse odalira pa cipulumutso cake. Tikuyamikani kaamba ka Mphatso yaikulu! Mutikhululukire umbombo wathu. Mutithandize kukhala okonda kupatsa mwa cikondi canu. M'dzina lanu tikupemphani izi. Amen.

## 6. Ana a Mulungu amvera

*Taonani, kumvera ndiko kokoma koposa nsembe – 1 Samueli 15.22b*

**Kuwerenga**
Yohane 15.8-12

**Malongosoledwe**
Baibulo litiuza za mfumu wochedwa Sauli. Iye anali mfumu wa Aisrayeli anthu a Mulungu. Anali mwamuna wamkulu ndi wamtali. Analinso wolimba mtima. Anali msirikali wabwino. Anthu anakondwera pamene Mulungu adamsandutsa Sauli kukhala mfumu.
Tsiku lina Samueli mneneri wa Mulungu, anati kwa Sauli, 'Mulungu afuna kuti mupita kumenyera Aamaleke. Iwo anali oipa ndi wankhanza. Mutapambana simuloledwa kusunga zao: nkhosa iriyonse, ngamira iriyonse kapena nyama iriyonse. Muyenera kuzipha zonse.'
Sauli anasonkhanitsa asirikali onse ndipo anapita kumenya nkhondo. Mulungu anagwiritsa nchito Sauli kulanga Aamaleke oipa. Sauli ndi asirikali ake anapambana ndipo anali okondwera kwambiri.
Koma usiku Mulungu analankhula ndi Samueli. Anati, 'Sauli sadandimvere'.
Samueli anamva cisoni. Anaganiza pa cimene Sauli akadacita. M'mawa Samueli anapita ku misasa ya asirikali.
Pamene Samueli anabwera pafupi ndi misasa, iye anamva phokoso. Anaima kumvera. Anamva kulira kwa nkhosa ndi ng'ombe. Mosacedwa iye anadziwa zimene Sauli adacita!
Samueli anathamanga. Patapita kanthawi kang'ono anapeza Sauli. Sauli anakondwa poona Samueli. Anati, 'Ndidacita monga Mulungu andiuza'.
Koma Samueli anati, 'Bwanji za phokoso la kulira kwa nkhosa ndi ng'ombe limene ndili kumva?'.
'O', Sauli ananena, 'Asirikali anga anasunga nyama zabwino koposa. Afuna kupereka nyama izi kwa Mulungu. Afuna kuzipereka nsembe'.
Samueli anapukusa. 'Mulungu adakuuzani kusasunga nyama iriyonse', iye anati. 'Ndipo cifukwa ca kusamvera kwanu, Iye adzacotsa ufumu wanu kuli inu.'
Pa nthawi iyo Sauli anamva cisoni. Anacedwa kwambiri kuphunzira kuti kumvera Mulungu ndi kofunikira kwambiri. Kumvera ndi kofunikira kuposa ngakhale kupatsa kwa Mulungu. Ganiziraniko!
Tingapatse Mulungu ndalama zambiri. Tingampatse mphatso zazikulu. Koma ngati timkondadi tizimumvera. Kumvera ndiko njira yofunikira koposa kumuonetsa kuti timkonda.
Mulungu anapatsa lamulo lapadera limene ana azikumbukira. Anati kwa ana, 'Mverani akukubalani mwa Ambuye'. Ici citanthauza, mverani makolo anu cifukwa Mulungu afuna kuti muziwamvera. Ngati muwamvera, mumvera Iye. Yesu anamvera makolo ake pa dziko lapansi ndipo anamveranso Atate wake Kumwamba.
Tiyenera kukula m'kumvera.

**Kukambirana**
1. Cifukwa ciani Sauli sanamvere Mulungu?
2. Kodi Mulungu anamva bwanji za kusamvera kwa Sauli?
3. Kodi ndi cotheka kuti tikonda Mulungu moonadi koma sitimumvera?
4. Patsani zitsanzo zisanu za kusamvera kwa Mulungu.
5. Cifukwa ciani ana azikonda makolo ao?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Yesu Kristu, Munamvera Atate wanu nthawi zonse. Mutisunge pafupi nanu kuti tiphunzire kumveranso nthawi zonse. M'mitima yathu muli zoipa zambiri, makamaka kusamvera cifuniro canu. Mutikhululukire kusamvera kwathu. Tipatseni Mzimu wanu Woyera kutiphunzitsa kukhala osangalala mwa kucita cifuniro canu. Tikupemphani izi mwa cisomo, m'dzina lanu. Amen.

## 7. Ana a Mulungu agwira nchito

*Masiku asanu ndi limodzi uzigwira, ndi kumariza nchito zako zonse – Eksodo 20.9*

**Kuwerenga**
2 Atesaloniki 3.10-12

**Malongosoledwe**
Kodi munaona tiana ta mphaka kusewera? Tiana ta mphaka tikonda kuthamanga ndi kujumpha. Tikonda kusewera ndi mpira. Tikonda kuzungulira padothi.
Tinyama tina timaseweranso, mwacitsanzo tiana ta agalu, tiana ta mikango ndi tiana ta nkhosa. Ito tonse timasewera.
Ndiponso ana akonda kusewera.
Koma ana ayeneranso kugwira nchito. Ana saloledwa kusewera nthawi zonse. Anyamata ndi atsikana atakula, iwo ayenera kuthandiza amai ndi atate kugwira nchito. Ngati akula koposa, kuli nchito zina zimene ayenera kucita. Anthu akulu azigwira nchito nthawi zonse. Ayenera kugwira nchito cifukwa ndiko kulingana ndi cifuniro ca Mulungu.
Pamene Mulungu anapanga Adamu ndi Hava, Iye anawaika m'munda wokongola. Momwemo munali maluwa, mbalame, mitengo yobereka zipatso zosiyanasiyana ndiponso mitsinje yodzala ndi madzi abwino. Koma Adamu ndi Hava anayenera kugwira nchito. Mulungu anawauza, 'Muyenera kusamalira munda'.
Adamu ndi Hava anakondwa m'munda. Anakonda kugwira nchito. Cinali cinthu cowakondweretsa kusamalira mitengo ndi nkhalango ndiponso kusunga bwino munda wamkulu kuti uoneke bwino.
Koma uchimo unabwera. Mudziwa momwe Adamu ndi Hava anamvera Satana. Sanamvere Mulungu. Kucokera pa nthawi iyo, nchito inali yobvuta. Mulungu anatulutsa Adamu ndi Hava m'munda. Iwo anayenera kukumba nthaka. Anayenera kudzala mbeu. Anayenera kucotsa mbeu zosafunika. Mbeu zosafunika zimakula msanga! Ndipo kunali munda wodzala ndi minga imene inabaya.
Ifenso tiyenera kugwira nchito molimba nthawi zina. Ndipo nthawi zina nchito itilemetsa. Koma nchito itikomera.
Nchito itilimbikitsa. Pamene tigwira nchito, matupi athu akula kulimbika.
Nchito itikondweretsa. Tikonda kupanga zinthu. Kutsiriza nchito yathu mwaubwino ndiko manyado.
Tikhoza kugwira nchito kuthandiza anthu ena kuti akondwera.
Cabwino coposa ndi kuti tikhoza kugwira nchito kwa Mulungu. Ngati ticita bwino nchito yathu, Mulungu adzasangalala. Ndipo ngati tiganizira Iye pa nthawi ya nchito, tidzakondwera, nchito ingakhale yobvuta. Kugwira nchito kwa Mulungu ndiko kodabwitsa.
Kusamalira cilengedwe ca Mulungu (mbalame, mitengo, maluwa ndi nyama) ndiko mbali ya nchito zimene tiyenera kucita.

**Kukambirana**
1. Cifukwa ciani tiyenera kugwira nchito?
2. Patsani zifukwa ziwiri za ubwino wa kugwira nchito.
3. Kodi tingagwire nchito bwanji kwa Mulungu?
4. Kodi tingacitire ciani anthu ena kuti asangalatse?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wa Kumwambamwamba, Tifuna kukuyamikani kuti mutipatsa mphamvu yogwira nchito kuti tidye. Mutikhululukire ngati tinakhala aulesi kapena osakonda nchito. Mutithandize kucita nchito zathu ku ulemerero wanu. M'dzina la Yesu tikupemphani, Amen.

## 8. Ana a Mulungu awerenga Baibulo

*Mau anu anakhala kwa ine cikondwero ndi cisangalalo ca mtima wanga – Yeremiya 15.16b*

**Kuwerenga**
Deuteronomo 11.18-21

**Malongosoledwe**
Pamene anyamata ndi atsikana apita ku sukulu, aphunzira kuwerenga. Aphunzira kuwerenga mabuku. Kuli mabuku abwino ambiri kuwerenga. Kuli mabuku zikwi ndi zikwi. Ndipo tifuna kuwerenga mabuku abwino cifukwa kuli zambiri tingaphunziremo.
Kuli Buku limodzi limene anthu onse ayenera kuwerenga. Bukuli ndi Baibulo. Baibulo ndi Buku lofunikira kuposa mabuku ena onse. Cifukwa ciani Baibulo ndi Buku lofunikira koposa?
Cabwino, Bukuli ndi Buku la Mulungu. Ndi Bukuli lokha limene Mulungu anatilembera. Ndi Buku lokha limene litiuza m'mene tiliri ndi cifukwa cace ca kukhala pa dziko lapansi. Kopanda Baibulo sitingamvetse konse ciriconse!
Kale pa nthawi ya Mose, Mulungu anayamba kulemba Baibulo. Mukumbukira nthano za Mose. Pamene anali mwana wa khanda, mai wake anamuika m'kabokosi m'mtsinje ndipo mwana wamkazi wa Farao anampeza. Mose anasanduka mtsogoleri wamkulu wa anthu a Mulungu.
Mose uyu anali mwamuna wokonda kwambiri Mulungu. Kawiri anakhala pamodzi ndi Mulungu pa phiri masiku makumi anai.
Mulungu anagwiritsa nchito Mose kuyamba kutilembera Buku lake. Mulungu Mzimu Woyera anatsogolera Mose mwa kumuuza zimene ayenera kulemba. Mose analemba zonse za momwe Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi ndiponso momwe Mulungu adalenga zonse za pa dziko lapansi. Analemba za Adamu ndi Hava, za kulengedwa kwao kodabwitsa ndi momwe sanamvere Mulungu. Mose analemba za Aisrayeli anthu a Mulungu, momwe Mulungu anawapangitsa kukhala anthu ake ndi momwe anawasamalira.
Kenaka Mulungu anasankha amuna ena kulemba zina zambiri. Iwo anauza za Mpulumutsi womwe adzabadwa. Tiwacha amunayo 'aneneri'.
Kenaka Mulungu anasankhabe amuna ena kulemba momwe Mpulumutsi adabwera ndi zimene adaticitira. Amuna ena a iwo anali ophunzira a Yesu.
Baibulo ndi Buku lalikulu. Sitikwaniritsa kuwerenga zonse pa tsiku limodzi. Tsiku ndi tsiku tiziwerenga mbali yaing'ono. Mwa kucita tero tidzaphunzira zonse za Iye zimene Mulungu afuna kuti tidziwe. Baibulo ndi Buku lodabwitsa kotero kuti tingawerenge mbali yaing'ono tsiku ndi tsiku mpaka takalamba kwambiri ndipo nthawi zonse tidzaphunzirabe zina za Mulungu. Tidzaphunzira ukulu wa Mulungu ndiponso momwe tikhoza kukhala miyoyo yathu kwa Iye.
Kuphunzira mau a pa mtima a m'Baibulo ndiko kwabwino.
Motero tidzakula m'njira zonse zabwino.

**Kukambirana**
1. Cifukwa ciani Baibulo ndi Buku lapadera?
2. Kodi mumawerenga Baibulo?
3. Kodi tiyenera kucita ciani ngati sitimvetsa mbali ina ya m'Baibulo?
4. Salimo 119.105 ikamba kuti, 'Mau anu ndiwo nyali ya ku mapazi anga, ndi kuunika kwa panjira panga'. Fotokozani ndime iyi.

**Citsanzo ca pemphero**
Tikulemekezani, Mulungu wamkulu kuti mutipatsa Baibulo kuti tikudziweni. Kopanda Mau anu ndife otayika cifukwa momwemo tiphunzira za Yesu Kristu Mpulumutsi weniweni. Tipatseni Mzimu Woyera kuti timvetsetse Baibulo. Mutikhululukire kuti nthawi zambiri sitikonda kuwerenga Baibulo. Tithandizeni kuphunziramo tsiku ndi tsiku pamodzi ndi banja lathu. Tikupemphani izi m'dzina la Yesu, Amen.

## 9. Ana a Mulungu amganizira Iye

*Inu mudzasunga mtima wokhazikika mu mtendere weni weni, cifukwa ukukhulupirirani Inu – Yesaya 26.3*

**Kuwerenga**
Salimo 77.11-14

**Malongosoledwe**
Kodi munamva za Davide, mnyamata wowetera nkhosa? Baibulo litiuza za iye. Iye anasungira nkhosa za tate wake. Davide anayenda kutali ndi nkhosa kuzipezera udzu wabwino. Nthawi zina anazitengera ku cigwa ca udzu pakati pa mapiri. Anaziyang'anira tsiku lonse. Pamene nkhosa zinamva ludzu, anazitenga ku madzi odikha kuti zimwe. Nthawi zonse analondolera kuona ngati kunabwera cilombo cacikulu (monga mkango) cimene cimafuna kugwira nkhosa kapena mwana wa nkhosa.
Nthawi zina pamene nkhosa zimapumula, Davide anali ndi mpata kukhala pansi. Pa nthawi iyo iye anatenga zeze yake nayamba kuiimba. Davide anapanga chamba yabwino ndi zeze yake ndipo analemba nyimbo zambiri. Davide analemba nyimbo zambiri za Mulungu.
Mwaona, Davide anaganizira Mulungu nthawi zonse. Anayang'ana mapiri omzungulira naganizira Mulungu amene anaika mapiri kumeneko. Pamene anaona maluwa pa udzu, iye anaganizira Mulungu amene analenga maluwa ooneka bwino ndi okongola kwambiri. Usiku pamene nkhosa zinali m'khola, Davide anayang'ana pamwamba kuona nyenyezi. Pa nthawi iyo anaganizira ukulu wa Mulungu ndiponso kuti Mulungu ndi wolemekezeka ndi woyera.
Davide anaganizira Mulungu nthawi zambirimbiri. Kotero anakula kukhala mtumiki wamkulu wa Mulungu. Ndipo Mulungu anakonda kwambiri Davide.
Tiziganizira za Mulungu tsiku ndi tsiku ndiponso nthawi zambiri pa tsiku lirilonse. Ngati timganizirako pa nthawi ya nchito ndi yosewera, tidzayesa kumkondweretsa. Tiyenera kuyesa kusangalatsa Mulungu (Atate wathu) ndi Yesu (Mpulumutsi wathu) wokondedwa, m'zonse zimene ticita. Kotero ifenso tidzakula kukhala ana a Mulungu oima nji.
Ngati tiganizira Mulungu pa nthawi yosewera, sitidzakhala odzikonda, okwiya kapena okalipa. Tidzakhala okoma mtima, acikondi ndi abwino. Ngati tiganizira Mulungu pa nthawi yogwira nchito, tidzagwira nchito mwaubwino. Kumbukirani, Iye ndi Atate wathu wa Kumwamba amene atikonda kwambiri. Ndipo Yesu, Mpulumutsi wathu wokondedwa, atikondanso kwambirimbiri.
Ngati timamganizira nthawi zambiri, tingakhale osamvera kodi? Kapena tingaope, ngakhale usiku, kodi?
Akristu aziganizira Mulungu nthawi zambirimbiri. Ayenera kuimba matamanda ake pamene akumbukira momwe Iye awakonda. Kotero iwo adzakhala Akristu okondwera.
Paulo mtumiki wamkulu anati, 'Pakuti kwa ine kukhala ndi moyo ndiko Kristu'. Cikondi ca Yesu cinadzala mtima wake kotero kuti anakhala moyo wake wonse kwa Yesu. Cifukwa cake anakondwera ngakhale pa nthawi ya mabvuto. Mtima wake unali wodzala ndi maganizo a Yesu.
Kuganizira Mulungu kulimbikitsa mitima yathu yatsopano kukula mwa cikondi ndi ciyero.

**Kukambirana**
1. Kodi Davide anacita ciani pa nthawi yoweta nkhosa?
2. Kodi mukonda kuganiza za Mulungu?
3. Paulo ananena kuti kukhala ndi moyo ndiko Kristu. Kodi ici citanthauza ciani? Nanga kukhala moyo wanu ndiko ciani?
4. Davide analemba Salimo 51. M'ndime ya 11 Davide ananena, 'Musandicotsere Mzimu wanu Woyera'. Davide anafunika Mzimu Woyera kumtsogolera m'moyo wake wauzimu. Nanga inu, mufunanso Mzimu Woyera kukutsogolerani?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Mulungu, Mutikhulululukire pakuti nthawi zambiri sitiganizira za Inu. Ndife ocimwa ofunika Mzimu Woyera kutitsogolera. Tiyeretseni ndi kuonetsa njira zanu. M'dzina la Yesu tikupemphani izi, Amen.

## 10. Ana a Mulungu aphunzira kukana

*Cotsalira, tadzilimbikani mwa Ambuye – Aefeso 6.10a*

**Kuwerenga**
Danieli 3.19-29

**Malongosoledwe**
Nthawi zina ana a Mulungu ayesedwa kucita coipa. Kodi mudziwa zimene muyenera kunena ngati munthu akuuzani kucita coipa? Muyenera kunena 'Iai!'
Nthawi zina ndi cobvuta kwambiri kunena 'iai'.
Tsiku lina, kale kwambiri, mfumu woipa anapanga fano lalikulu. Anauza anthu ake onse kuti ayenera kugwadira fano. Anati kuti ndilo mulungu.
Anthu onse anasonkhana ku mbali zonse za fano. Kunali anthu ambiri. Kenaka mtumiki wa mfumu anapfuula, 'Pamene mukumva mau a zoimba, inu nonse muyenera kugwada!'
Mosacedwa zoimba zinayamba kulira. Kodi iwo onse anagwada kupembedza fano ngati mulungu? O, iai! Osati anthu onse. Anyamata atatu s
Indedi, mfumu anakalipa pam ika mtima kuima ngakhale ndawauza kuti ayenera kugwada, ndiwo yani? Abweretseni kwa ine!'
Atumiki ake anabweretsa anyamata atatu: Sadrake, Mesake ndi Abedinego.
Mfumu anawauza, 'Ndiri ndi ng'anjo ndi moto wotentha kwambiri. Ngati musagwadira fano langa, ndidzakuponyani m'ng'anjoyo. Tsopano zoimba zidzaimbanso ndipo muyenera kugwada pansi!'
Anyamata anapukutsa mitu yao. Anati, 'O, iai mfumu. Titumikira Mulungu wamoyo. Sitikhoza kugwadira fano ndi kucimwira Mulungu wathu. Pamene zoimba zilira, sitidzagwada pansi ndipo Mulungu adzatisamalira.'
Iwo anali anyamata olimbika mtima. Analimba mtima kunena 'Iai' kwa mfumu. Ici sicinali capafupi! Anadziwa kuti mfumu adzawaponya m'moto wotentha.
Ndipo mfumu anacita tero. Anakalipa kwambiri! Koma o, ndi cinthu codabwitsa! Mulungu anatuma mngelo kuwasamalira. Ndipo moto sanawapweteke konse!
Baibulo litiuza za anyamata awa atatu cifukwa iwo anali olimba mtima kunena 'iai'. Ndipo Baibulo litiuza kuti Nebukadinezara mfumuyo wamkulu analemekeza Mulungo poona momwe Mulungu anasamalira anyamata olimba mtima.
Nthawi zina tiyenera kunena 'iai'.
Nthawi zina tifuna kucita cimene amai atiletsa. Pa nthawi iyo tiyenera kunena 'Iai, sindidzacitira mwano amai'.
Nthawi zina anzathu atiyesa kucita coipa. Pa nthawi iyo tiyenera kunena 'iai'.
Nthawi zina Satana ayesa kutipangitsa kukhala osamvera amai kapena atate. Pa nthawi iyo tiyenera kunena 'iai'.
Nthawi zonse pamene tiyesedwa kucita coipa, tiyenera kunena 'iai'. Motero tidzakhala ana olimbika a Mulungu.

**Kukambirana**
1. Cifukwa ciani anyamata atatu sanagwadire fano?
2. Kodi kuyesedwa kutanthauza ciani?
3. Kodi mumacita ciani ngati munthu afuna mucimwira Mulungu?
4. Kodi tiyenera kucita ciani pamene kukana ndi kobvuta?
5. Mulungu akamba kuti, 'Koma ngati diso lake lamanja likulakwitsa iwe, ulikolowole, nulitaye; pakuti nkwabwino kwa iwe, kuti cimodzi ca ziwalo zako cionongeke, losaponyedwa thupi lako lonse m'gehena'. Kodi ndime iyi itanthauza ciani?
6. Cifukwa ciani tifunika mphamvu ya Mulungu kupewa mayesero? Cifukwa ciani sitikwaniritsa kupewa mayesero mwa mphamvu yathu (Yakobo 1.14 ndi 15)?

**Citsanzo ca pemphero**
Atate wathu wa Kumwamba, Nthawi zambiri tiyesedwa kukucimwirani. Mitima yathu ndi yocimwa. Mutithandize kuima nji kuti tipewa mayesero ndi kukukondweretsani. Tidziwa kuti Ambuye Yesu anapewa mayesero onse; mutisunge mwa Iye kuti ndife oyera pa maso panu. Tikupemphani m'dzina lake, Amen.

## 11. Ana a Mulungu auza nthano ya Mulungu

*Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse – Mateyu 28.19a*

**Kuwerenga**
Mateyu 28.16-20

**Malongosoledwe**
Simoni ndi mbale wake Andreya anapita kuwedza nsomba. Anali ndi ngalawa pa Nyanja ya Galileya. Ndipo anali ndi khoka. Nthawi zonse ankagwiritsa nchito makoka powedza nsomba.
Iwo atayendetsa bwato kucokera ku mbali ya nyanja, anaika kokha m'madzi. Simoni anagwira mbali ya kokha. Andreya nayenso mbali ina.
Mwadzidzidzi pamene anali kuyang'anira kokha, anamva munthu popfuula, 'Simoni! Andreya!'
Anaona mwadzumwadzu naona Munthu pokhala pa mbali ya nyanja. Ndi Yesu. Anawaitana. 'Bwerani, ndilondoleni!', Yesu anati, 'Ndipo ndidzakusandutsani asodzi a anthu'.
Asodzi a anthu? Simoni ndi Andreya sanadziwe cimene Yesu anatanthauza. Koma anatenga kokha lao nayendetsa ngalawa ku mbali ya nyanja. Anacoka m'ngalawa yao napita pamodzi ndi Yesu.
Pafupi nao kunali amuna ena m'ngalawa ina. Yakobo ndi mbale wake Yohane anali kusoka makoka ao. Tate wao, Zebedayo, anali nao. Yesu anaima pa ngalawa yao nanena 'Bwerani, ndilondoleni!' Kenaka Yakobo ndi Yohane anasiya makoka ao natsata Yesu. Yesu anafuna Simoni, Andreya, Yakobo ndi Yohane kukhala asodzi a anthu. Kodi mudziwa kuti ici citanthauza ciani?
Kucokera kwa nthawi ya unyamata wao, iwo anali kuwedza nsomba m'makoka ao. Anabweretsa nsomba ena kunyumba kukhala cakudya cao. Anagulitsa nsomba zina. Anadziwa bwino za kuwedza nsomba mogwiritsa nchito makoka.
Tsono Yesu anawauza kuti ayenera kuwedza anthu ndi kuwabweretsa m'Ufumu wa Mulungu. Kuwedza kotere ndi kosiyana. Yesu adzawatuma m'dziko lonse lapansi kupeza anthu ndi kuwabweretsa kwa Iye.
Yesu anawasandutsa asodzi a anthu. Poyamba Yesu anawaphunzitsa za njira ya kuwedza anthu. Ndipo iwo anasanduka alaliki ndi atumiki. Anauza nthano ya cipulumutso kubweretsa anthu osiyana-siyana m'Ufumu wa Mulungu.
Yesu asanapite Kumwamba, anati kwa ophunzira ake onse, 'Mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse Uthenga Wabwino'. Ndiye anasandutsa iwo onse asodzi a anthu.
Ngati ndife a Yesu (ngati Mzimu Woyera akhala m'mitima yathu), ifenso tiyenera kukhala asodzi a anthu. Tiziuza anthu ena za Yesu, kuti adzabwera ku Ufumu wa Kumwamba. Kuli anthu ambiri amene sadziwabe Yesu ndipo sanamvere konse za cikondi cake codabwitsa. Iwo sadziwa kuti Iye anafa cifukwa ca macimo athu ndi kuti afuna kutisandutsa anthu ake. Tifuna kucita zonse zimene tikhoza kuwauza nthano yodabwitsa ya Mulungu. Pamene ticita tero, ndife asodzi a anthu.
Tikula pamene tiphunzira kukhala bwanji asodzi a anthu.

**Kukambirana**
1. Kodi kukhala asodzi a anthu kutanthauza ciani?
2. Kodi tingakhale bwanji asodzi a anthu?
3. Kodi tiyenera kuuza ciani za Yesu?
4. Kodi mungacita ciani kuti anthu ena adziwe ndi kukhulupirira Yesu?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Yesu Kristu, Zikomo kwambiri kuti mufuna anthu onse kudziwa Uthenga Wabwino wanu. Mutipatse Mzimu Woyera kukudziwani kotero kuti tifuna anthu enanso kukudziwani. Dalitsani iwo onse afalitsa ndi kulalikira Baibulo. Muwathandize kuti akhale okhulupirika, osalalikira maganizo ao koma Baibulo lanu. M'dzina la lanu tikupemphani. Amen.

## 12. Ana a Mulungu azunzika cifukwa ca Iye

*Odala muli inu m'mene adzanyazitsa inu, nadzazunza inu, nadzakunenerani monama zoipa ziri zonse cifukwa ca Ine – Mateyu 5.11*

**Kuwerenga**
Macitidwe a Atumwi 7.54-60

**Malongosoledwe**
Anthu a Mulungu ali okondwera kwambiri podziwa kuti Yesu awakonda. Koma nthawi zina ayenera kuzunzika cifukwa ca Yesu. Anthu ambirimbiri a Mulungu anabvutika cifukwa ca Yesu.
Atapita Kumwamba Yesu, ophunzira ake anayamba kuuza anthu momwe Yesu adafa cifukwa ca macimo athu. Anthu ambiri anakhulupirira Yesu. Anasanduka Akristu.
Stefano anali mwamuna wabwino. Anamva ophunzira kufalitsa nthano ya Yesu nakhulupirira. Mzimu Woyera anadzala mtima wa Stefano kotero kuti Stefano anakonda Yesu kwambiri. Kenaka Stefano anayamba kuuza anthu ena za Yesu. Anafuna anthu onse kudziwa nthano yodabwitsa. Anasanduka 'msodzi wa anthu'!
Anthu oipa amene adapha Yesu, anamva Stefano kulalikira za Yesu. Sanafune anthu enanso kukhulupirira. Ndiye analembera amuna ena kuuza mabodza a Stefano.
Amunawa ananena, 'Stefano ndi mwamuna woipa. Auza zinthu zoipa za Mulungu, zinthu zoipa ndithu'.
Stefano sanaope. Anapitiriza kuuza anthu kuti Yesu yekha ndi Mpulumutsi ndiponso kuti anthu onse ayenera kumkhulupirira.
Koma amuna oipa anagwira Stefano namkhwekhwereza kunja kwa mudzi. Anamponya pa njira. Anayamba kumponyera miyala. Anapitiriza kuponya miyala yaikulu mpaka anapha Stefano.
Anzake a Stefano sanakhoze kumthandiza. Anakhoza kuyang'ana cabe. Anaona Stefano kugwada iye asanafe. Anaona kuti Stefano anapenya Kumwamba ndipo anaona nkhope yake kuwala ngati nkhope ya mngelo! Anamva kuti Stefano ananena, 'Ndiona Yesu!' Ndipo anamva kuti ananena, 'Ambuye Yesu, landirani mzimu wanga'. Kenaka Stefano anafa.
Anzake analira pamene anaika Stefano m'manda. Anamva cisoni kwambiri cifukwa ca kuzunzidwa kwa Stefano. Koma anadziwa kuti Stefano sadakhoze kuleka kuuza za Yesu, ngakhale miyala ingapweteke kwambiri. Anadziwa kuti mtima wake unali wodzala ndi cimwemwe pamene anaona Yesu. Anadziwanso kuti, angakhale iwo aika thupi lake m'manda, mzimu wa Stefano ali pafupi ndi Yesu.
Ciani cimene cinapangitsa anthu oipa kuda Stefano kwambiri? Satana adadzala mitima yao ndi kuda. Satana ndi mdani wa Mulungu, monga mudziwa. Iye safuna ife kuuza za cikondi ca Mulungu ndi cikondi ca Yesu.
Yesu adauza ophunzira ake kuti iwo adzazunzika cifukwa ca Iye. Adawauzanso kuti kuzunzidwa kungawasangalatse.
Mkristu ayenera kukonda Mulungu ndithu kuti angazunzike cifukwa ca Iye.

**Kukambirana**
1. Cifukwa ciani anthu anafuna kupha Stefano?
2. Kodi tiyenera kuleka kulankhula za Mulungu pamene anthu atiletsa?
3. Kodi Stefano anaona ciani comkondweretsa?
4. Kodi kusiyana kwa kuzunzika cifukwa ca Yesu ndi kuzunzika cifukwa ca makhalidwe athu ndiko ciani?
5. Mulungu akamba kuti, 'Ndipo onse akufuna kukhala opembedza m'moyo mwa Kristu Yesu, adzamva mazunzo' (2 Timoteo 3.12). Kodi tingayankhe bwanji anthu amene anena kuti Akristu oona sabvutika?
6. Yesu ananena, 'Onani, ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano' (Mateyu 28.20b). Kodi mau awa alimbikitsa bwanji anthu ozunzika cifukwa ca Iye?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Yesu, Nthawi zambiri tiopa kuti anthu angatizunze cifukwa ca Inu. Sitifuna mabvuto. Koma ngati mufuna kuti tibvutika cifukwa ca Inu, mutipatse mphamvu kukhala olimba ndi okondwera mwa Inu. Tikuyambikani kuti musasiya konse ana anu. Limbikitsani iwo onse ozunzika cifukwa ca Inu. Tikupemphani mwa cisomo m'dzina lanu. Amen.

## 13. Ana a Mulungu afunafuna za tsogolo

*Zimene diso silinaziona, ndi khutu silinazimva, Nisizinalowa mu mtima wa munthu, Zimene ziri zonse Mulungu anakonzereratu iwo akumkonda*
*Iye – 1 Akorinto 2.9b*

**Kuwerenga**
1 Yohane 3.1-3

**Malongosoledwe**
Pamene Paulo mtumiki wamkulu wa Mulungu anakhala wokalamba, iye anaikidwa m'ndende m'Roma. Analimo nthawi yaitali. Wolamulira woipa a Roma anaika asirikali omyang'anira. Patapita nthawi iye anapha Paulo.
Kodi Paulo anacita zolakwa? O, sanaikidwe m'ndende cifukwa ca colakwa. Anaikidwa m'ndende cifukwa analalikira za Yesu, monga Stefano anacita. Anthu amene anada Mulungu, anafuna kuletsa Paulo kulalikira nthano ya Yesu. Cifukwa cace, iwo anauza mabodza a iye namuika m'ndende.
Kodi muganiza kuti Paulo anacita ciani m'ndende?
Anapitiriza kulankhula za Yesu. Anauza ngakhale asirikali omyang'anira nthano ya Yesu. Anzake anabwera kumuona ndipo anawauza za Yesu. Analembera mamembala a mipingo makalata akulu nawauza momwe ayenera kukhala kwa Yesu ndi momwe ayenera kukhala osangalala mwa Yesu.
Paulo sananyinyirikire mabvuto ake. Kodi mudziwa cimene ananena? 'Mabvuto anga sakhala ofunikira konse. Adzakhala nthawi yaing'ono ndipo ndifunafuna zinthu zodabwitsa zimene Mulungu adzandipatsa pamene mabvuto onse atsira'. Anati, 'Ndikayenera kufa, ndidzapita kwa Yesu ndipo ico ndi cinthu cabwino koposa cimene cingacitike pali ine! Yesu anauka kwa akufa ndipo adzandiukitsa kwa akufa. Adzandipatsa thupi latsopano. Ndipo ndidzakhala moyo naye m'ulemerero muyaya!'
Kukhala mwana wa Mulungu ndi kodabwitsa. Mwana wa Mulungu angakondwere paliponse. Ngati tikomana ndi mabvuto, tidziwa kuti adzakhalitsa nthawi yaing'ono cabe. Tidziwa kuti atikometsa. Tiganiza za tsogolo. Tiganizira malo Kumwamba amene Yesu atikonzera.
Paulo anadziwa kuti adzafa. Koma sanamve mantha. Anali wotsimikiza kuti Yesu sadzaleka kumkonda. Anali wotsimikiza kuti Yesu adzamtenga Kumwamba. Anaona zinthu zabwino za kutsogolo nakhala wokondwera.
Ifenso tiyenera kuona kutsogolo. Kotero mazunzo a lero sadzatipangitsa kukhala osasangalala. Palibe bvuto ngati ndife osauka. Tsiku lina tidzakhala olemera! Ndife olemera ngati tiri ndi Yesu. Palibe bvuto ngati ndife odwala. Tidzakhala bwino ndipo sitidzadwalanso Kumwamba. Palibe bvuto ngati anthu atimsekera. Tidzakhala okondwa pamodzi ndi Yesu pamene atitenga kukhala nafe.
Mulungu anaticitira kale zinthu zodabwitsa. Anatipatsa njira ya cipulumutso mwa Yesu. Ndipo kuli zinthu zina zambiri za kutsogolo. Zinthu zabwino zotero kuti sitingafanizire momwe ziliri.
Pamene tiganiza za zinthu izi zonse, tifuna kukhala bwino; tifuna kukula ndi kukhala monga Yesu.

**Kukambirana**
1. Kodi Paulo anayankha bwanji mazunzo ake?
2. Nanga inu mukumva bwanji pa nthawi ya mabvuto?
3. Kodi ndinu m'modzi wa anthu ake otembenuka mtima amene adzakhala Kumwamba?
4. Ndife okonzeka pa nthawi ya imfa yathu ngati Mulungu anatikhululukira macimo athu mwa Yesu. Kodi mwalapa ku macimo anu ndi kulandira Yesu?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wamkulu, Ulemerero wanu ndi waukulu. Sitikhoza kufanizira momwe tsogolo la ana anu liliri. Mudziwa zimene ziri m'mitima yathu. Tikupemphani kuti mutikonzere kukhala Kumwamba. Tikupemphani m'dzina la Yesu Mpulumutsi, Amen.